

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

KUSALA KWA M'BAIBULO

Munthu wina wotchedwa Arthur Wallis ananena kuti, “Kusala ngati kukuchitika kuchokera mu mtima wona ndi cholinga cholondola, kukhoza kutipatsa ife makiyi otsegulira zitseko zimene zinali zotsekeka zomwe makiyi ena alephera. Kukhoza kukhalanso ngati mazenera otisekulira ife ku miyamba yatsopano m'dziko losaoneka, kapenanso zida zauzimu za Mulungu zimene zili, ‘zaphamvu mwa Mulungu zakupasula malinga.”

Machitidwe a zinthu mu Chipangano Chakale ndi Chatsopano

Kusala chakudya chifukwa chofuna kupindula ku uzimu ndi chinthu chimene oyera mtima a ku Chipangano Chakale ndiponso Chatsopano anali kuphunzitsa komanso kuchita. Mbiri imationetsa kuti abambo ndi amai odziwika bwino pa zinthu zauzimu anali kusala. Mu gulu limeneli muli Mose yemwe anapereka malamulo, Davide mfumu yotchuka ija, Eliya mneneri uja, Mfumukazi Estere, Anna mneneri wamkazi, Yesu mwana wa Mulungu, ndiponso Paulo mtumwiyo. Kusala ndi njira yoyeretsa maganizo komanso mzimu wathu modzichepetsa pamaso pa Mulungu, ndipo kumatsekula khomo lakuti munthu ulumikizane mozama ndi Ambuye. Palibe phindu lililonse kuuzimu ngati kusalako kuli kwa kuthupi chabe. Kuyambira kale ndithu, kwa anthu ambiri kusala chinali chinthu chongochitika kunja basi. Zinthu zooneka zauzimu pazokha sizinakwanitse kutisendezera chifupi ndi Mulungu. Mu magawo onse a kudzipereka ku uzimu, zinthu zochitika moonetsa kunja zili za mphamvu molingana ndi mzimu wamkati umene ukufunitsitsa kukondweretsa Ambuye mwa kudzichepetsa ndi mwachiyero. John Wesley anati, “Anthu ena amalemekeza kusala kwa uzimu kuposera malemba ndi zinthu za luntha, ndipo enanso sakulabadira nkomwe.” Pali mchitidwe wa mu Baibulo wa kusala umene uli waphindu kwambiri kwa ana a Mulungu ngakhale lero lino.

Tanthauzo lenileni

Mau akuti “kusala” akhala ali ndi matanthauzo osiyanasiyana ndipo anthu ambiri agwiritsa ntchito mauwa pofuna kunena za mchitidwe uliwonse odzikaniza ndi kulimana thupi mwa njira inayake. Ngakhale kuti Akhristu akuyenera kuchita momverera ndi modziletsa, mau akuti “Kusala” pamene apezeka m'Baibulo amatanthauza kwenikweni kudzikana chakudya.


Nkofunikira kuti tisachotsere kapena kuonjezera tanthauzo limeneli lomwe likuoneka ngati lophweka.

Chizindikiro cha kulira

Kusala kunali ngati chizindikiro choonetsa kulira, kukhudzidwa komanso chisoni. Pamene mfumu Saulo anafa, ndipo uthenga unamupeza Davide, Davideyo anasala mpaka madzulo (2 Samuele 1:11-12) ndipo ena anasala kwa masiku 7 poonetsa kulira ndi kupereka ulemu (1 Mbiri 10:11-12).

Kusala kolamulidwa ndi Mose kwa pa tsiku la chitetezero

Pansi pa chilamulo cha Mose, kusala kwa tsiku limodzi kwa pa “Tsiku la chitetezero” kunali kusala kokhako kodziwika kwa anthu onse kumene kunalamulidwa ndi Mulungu. “Komatu, tsiku lakhumi la mwezi uwu wachisanu ndi chiwiri, ndilo tsiku la chitetezero; mukhale nao msonkhano wopatulika, ndipo mudzichepetse ... Musamagwira ntchito iliyonse tsiku limenelo; pakuti ndilo tsiku la chitetezero” (Levitiko 23:26-32). Mau akuti, “ndipo mudzichepetse” amawatanthauzira kuti kusala chakudya. Izi zimayimirira kulira mwachisoni ndiponso kukhala ndi mzimu wodzichepetsa pamaso pa Mulungu. Davide “analira pa kusala kwa moyo wake” (Masalmo 69:10). Pa tsiku la chitetezero, kusala kumatsagana ndi kupereka chopereka ndipo limakhala tsiku lomwe anthu



“Kusala ndi njira yoyeretsa maganizo komanso mzimu wathu modzichepetsa pamaso pa Mulungu, ndipo kumatsekula khomo lakuti munthu ulumikizane ndi Ambuye mozama.”

(Yapitirira pa tsamba 2)

Nkhani Yotsagana
Nayo: Kusala kwa
M'baibulo

1-2, 5-6

Mau a Mkonzi

Mitundu inai ya
kusala

3

Kusanthula Baibulo:
Kusala

4

Mafunso ndi
Mayankho
Kumasulira
Baibulo m'njira ya
Interpolation

7

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

8

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

samagwira ntchito. Ayuda a mu Chipangano Chatsopano anapitiriza kukumbukira kusala kumeneko (Ntchito 27:9).

Kusala kanai pachaka kwa Ayuda

Kuphatikizapo pa tsiku la kusala pamene mau a Ambuye amawerengedwa (Yeremiya 36:6), panalinso mwambo wosala kanai pa chaka umene Ayuda amatsata pofuna kukumbukira nthawi zinai zimene mzinda wa Yerusalemu unaonongedwa. (Zekariya 8:19). Kupatula pa nthawi izi zoikika zosala, kusala mu Chipangano Chakale kumachitika ndi munthu payekha pokhapokha pakhale chinthu chochititsa kuti anthu asale ngati gulu. Nyengo za kusala ku Chipangano Chakale zimatipatsa popondera ndi chithunzithunzi cha mphamvu ndiponso cholinga cha kusala masiku ano.

Kusala kwa chigulu

Nthawi yoyamba imene kusala kwa gulu monga mwambo wachipembedzo kukutchulidwa pa Oweruza 20:26. Ana a Israele anali panthawi yankhondo ndipo anabwera ku nyumba ya Mulungu “nalira misozi, nakhala pansa pomwepo pamaso pa Yehova, nasala chakudya tsiku lomwelo mpaka madzulo.” Mulungu analowererapo ndipo anawapatsa chigonjeto. Chimodzimidzinsu, pamene Jehosafati anathedwa, analirira kwa Mulungu pamene adani anabwera kudziko la Yuda kuti alilande. Iye “nalalikira kusala mwa Ayuda onse” ndipo anthuwo anabwera kudzafunafuna Mulungu ndi kupempha kuti Iye awathandize (2 Mbiri 20:2-7). Poyankha ku pempho lao, Mulungu anati: “Musaope musatenge nkhwawa chifukwa cha aunyanji ambiri awa; pakuti nkhoodoyi si yanu, koma ya Mulungu... chilimikani, imani, nimupenye chipulumutso cha Yehova” (2 Mbiri 20:15-18).

Mphamvu ya kupempha

Mphamvu ya kupempha kudzera mu kusala ikupezekanso pamene Ayuda ku Babiloni anaopsezgedwa ndi lamulo lakuti aphedwa. Mfumukazi Estere analangiza Ayuda kuti asonkhane “nimundisalire, osadya osamwa masiku atatu, usiku ndi usana” (Estere 4:16-17). Mulungu analemekeza kusalako ndipo anawachitira chifundo anthu ake. Ezara ndi anthu obwera kuchokera ku ukapolo akubwerera kwao ku Yerusalemu anakumana ndi zoopsa panjira. M'malo mopempha kwa mfumu kuti apereke asilikali owaperekeza, Ezara anati “Pamenepo ndinalalikira chosala komweko kumtsinje wa Ahava, kuti tidzichepetse pamaso pa Mulungu wathu,” (Ezara 8:21-23). Mulungu anaonetseranso kuti amawerengera kusala ndi kupemphera.

Kusala kwa munthu payekha

Mfumu Davide anali ndi khalidwe lokonda kusala payekha. Iye anachepetsa moyo wake ndi kusala (Masalmo 35:11-13) kuti afunefune Mulungu kwambiri mu pemphero. Atachimwa ndi Bateseba, mwana waoyo anadwala mpaka kufa. Ndipo iye anati, “Pamene mwanayo akali ndi moyo, ndinasala kudya ndi kuliraKoma tsopano wafa, ndidzasaliranjinso kudya?” (2 Samuele 12:15-23).

Kusala kwa kulapa

Nthawi zambiri kusala kumalumikizana ndi kufunafuna Mulungu mwa kulapa. Mose anasala kwa masiku 40 chifukwa cha machimo a

(Yapitirira pa tsamba 5)

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvumere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Ndipo ndinaika nkhope yanga kwa Ambuye Mulungu, kumfunsa Iye m'pempheo, ndi mapembezera, ndi kusala, ndi ziguduli, ndi mapulusa. —Daniele 9:3

Ngati anthu a Mulungu ochuluka, abambo ndi amai omwe, akanatembenukira nkhope zao kwa Ambuye, namufunafuna Iye mu kusala ndi kupemphera, ndikutsimikizika mtima kuti tikanaona uzimu wochuluka, kudzoza kochuluka, komanso mphamvu zochuluka mwa Mulungu. Mutu umene tikulingalira ulendo uno uli pa nkhani ya kusala. Mutuwu wakhala ukusokonezedwa ndipo anthu ambiri saumvetsetsa komanso mchitidwewu sukuchitika kawirikawiri pakati pa anthu ambiri oyera mtima.

Kusala sikutanthauza kudzilanga kapena kuyesetsa kupinda mkono wa Mulungu pofuna kuti atichitire zimene ifeyo tikufuna. Kusala ndiwo mchitidwe wosweka mtima ndi kudzichepetsa pofuna kulemekeza Ambuye ndi kuyika pambali chakudya chathupi kwa kanthawi ndi kukhazikika pa zinthu za Mulungu. Ndife otanganidwa ndi kutakataka ndi zinthu za moyo uno—nchifukwa chake kusala kuli nthawi yakuti tikhazikike, tilingalire mozama ndiponso tidzipereke kwathunthu kwa Ambuye. Zimenezi zimalimbikitsa ubale wauzimu ndi kulumikizana ndi Mulungu ndipo izi zimapangitsa kuti Ambuye athe kugwira ntchito yake ndi kudziwulula yekha kwa ife monga m'mene tilili. Kusala kwenikweni kumakhala kofunikira pofuna kusintha kachitidwe ka zinthu m'dziko kudzera mu mphamvu ndi kulowererapo kwa Mulungu.

Ineyo ndakhala ndikulimbikitsidwa ndi malemba pa mutu umenewu ndipo ndikulimbikitsani ena nonse kuti timufunefune Ambuye kuti timvetsetse bwino, tikhulupirike ndi kudzipereka mu kusala.

Michael W. Smith

July 2018

Zambiri Zili pa
INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.

MITUNDU INAI YA KUSALA

KUSALA KWA UZIMU

Kusala kumene Mulungu amapereka mphamvu zapadera kuchokera kumwamba.

Moses anasala kwa nyengo ziwiri kwa masiku 40. Duteronomo 9:9, 18
Eliya sanadye kwa masiku 40. 1 Mafumu 19:8

KUSALA KWENIKWENI

Kuleka kudya zakudya zilizonse koma kumangomwa zinthu zamadzimadzi.

Kusala kwa Yehosafati. 2 Mbiri 20:3
Davide anasala chakudya. 2 Samuele 12:21
Yesu sanadye koma mwina anamwa madzi. Mateyu 4:2

KUSALA KWATHUNTHU

Osamwa madzi kapena kudya

Anthu a ku Nineve sanadye kapena kumwa. Yona 3:5-10 (Ezara 10:6)
Kusala ku chakudya ndi chakumwa. Estere 4:15-16
Saulo sanadye kapena kumwa. Ntchito 9:9

KUSALA KOMVERERA

Kudzimana kudya chakudya china chimodzi pa tsiku kapena mtundu wina wa chakudya.

Sanadye zosangalatsa kapena nyama. Daniele 10:2-3

Kusanthula Baibulo

Mutu: KUSALA

Kuwerenga malemba: Patulani tsiku losala, lalikirani masonkhano oletsa, sonkhanitsani akuluakulu, ndi onse okhala m'dziko, kunyumba ya Yehova Mulungu wanu; nimufuulire kwa Yehova. —Yoweli 1:14

Mwachidule: Kusala ndi mchitidwe wa kalekale ndithu umene anthu a Mulungu amachita kuyambira mu Chipangano Chakale ndi Chatsopano ndipo lili gawo lofunikira kwambiri la moyo wa Mkhirsitu masiku ano. Ndi chinthu chochitika kunja chimene chikhoza kutithandiza kuti malingaliro, matupi ndi mzimu wathu zikhazikike pa zinthu za Mulungu. Ndi njira imene zikhoza kudzeramo mphamvu za Mulungu za mamasulidwe, chitsogozo, kudzoza ndi kukula mu uzimu.

Tanthauzo: Ngakhale kuti Akhristu akuyenera kudzikana ku zinthu zina ku magawo ambiri, mu Baibulo mau akuti “Kusala” kwenikweni amatanthauza kudzikana chakudya.



I. Kusala kukulamulidwa pansu pa chilamulo cha Mose

- A. Levitiko 23:26-32 “Tsiku la chitetezero” linali tsiku lokhalo lolamulidwa ndi chilamulo kuti anthu asale (Levitiko 16:29-31, Numeri 29:7).
- B. “Mudzichepetse” kutanthauza kusala.
- C. Masalmo 69:10 Davide analira moyo wake ndi kusala.
- D. Ntchito 27:9 Ayuda a mu Chipangano Chatsopano amakumbukirabe kusala pa tsiku la chitetezero.

II. Mitundu inai ya Kusala kwa mu Chipangano Chakale

- A. Zekariya 8:19 Kusala kanai pachaka pokumbukira nyengo zikuluzikulu zokhudzana ndi kuonongedwa kwa mzinda wa Yerusalemu.

III. Zochitika komanso cholinga cha kusala mu Chipangano Chakale

- A. 1 Mbiri 10:12 Pa nthawi ya chisoni ndi imfa (2 Samuele 1:11-12).
- B. 2 Samuel 12:16-23 Davide pamene mwana wake anadwala.
- C. Masalmo 35:11-13 Davide anachepetsa moyo wake ndi kusala.
- D. Nehemiya 9:1-3 Kulapa pakuwerengedwa kwa malamulo (Yeremiya 36:6).
- E. Oweruza 20:25-26 Panthawi ya nkondo (1 Samuele 7:5-8).
- F. 2 Mbiri 20:3 Yehosafati pamene Yuda anazingidwa ndi adani.
- G. Ezara 8:21, 23 Matchona pamene amafuna chitetezo pa ulendo wao wobwerera.
- H. Estere 4:3,16 Kupulumutsidwa ku lamulo la imfa.
- I. Duteronomo 9:17-20 Mose chifukwa cha tchimo la Israele.

- J. Daniele 9:3-5 Daniele anavomereza machimo a Aisraele.
- K. 1 Mafumu 21:17-29 Ahabu kuti akhululukidwe.
- L. Yona 3:4-10 Nineve kuti Mulungu asinthe maganizo ake.

IV. Langizo ndi chitsanzo cha Khristu

- A. Mateyu 4:1-9 Yesu anasala panthawi ya kuyesedwa kwake komanso pokonzekera utumiki wake.
- B. Mateyu 6:5, 16-18 “Pamene” musala, osati “ngati” musala.
- C. Mateyu 9:14-17 Ophunzira a Yesu adzasala mtsogolomo.
- D. Marko 9:17-29 Mphamvu ndi chikhulupiriro zazikulu kudzera mu kusala ndi kupemphera (Mateyu 17:14-21).

V. Kusala mu mpingo wa Chipangano Chatsopano

- A. Luka 2:37 Khristu asanafike, Anna anali “kupembedza ndi kusala.”
- B. Ntchito 9:9 Saulo anasala kwa masiku atatu.
- C. 2 Akorinto 6:4-10 Paulo anali kusala pafupipafupi.
- D. Ntchito 13:1-3 Mpingo wa ku Antiokeya kuti utumize atumwi.
- E. Ntchito 14:21-23 Mpingo ya ku Galatiya ndi kudzoza akulu ampingo.

VI. Kusala kovomerezeka ndi kosavomerezeka

- A. Yesaya 58:3-6 Kusala kwa mwambo chabe mwathupi popanda kulapa kwenikweni ndi kosavomerezeka.
- B. Zekariya 7:1-14 Kusala kopanda kulapa kapena kosapereka ulemberero kwa Mulungu kuli kopanda phindu.
- C. Mateyu 6:16-18 Salani modzichepetsa.
- D. Yoweli 2:12-13 Ndi mtima wanu wonse.

Kumaliza

Koma adzafika masiku, pamene mkwati adzachotsedwa kwa iwo, ndipo pomwepo adzasala kudya.
—Mateyu 9:15

(Kuchokera pa tsamba 2)

anthu (Duteronomo 9:18). Mulungu anamusiya Ahabu osamulanga pamene Ahabuyo analapa nadzichepetsa mu mtima mwake pakusala (1 Mafumu 21:27-29). Anthu a ku Nineve anakhulupirira chiweruzo cha Mulungu monga analalikira Yona ndipo iwo anasala (ngakhale ndi nyama zomwe) ndipo anafunafuna Mulungu kuti asinthe maganizo ake. Mulungu analemekeza kusala ndi kulapa kwao ndipo anabweza mkwiyo wake pa iwo (Yona 3:5-10).

Daniele anayang'ana kwa Ambuye "kumfunsa Iye m'pempheo, ndi mapembedzero, ndi kusala" (Daniele 9:3). Iye anadzikhuthula nadandaulira kwa Mulungu kuti amuchitire chifundo chifukwa cha machimo a anthu ake. Ali mkati mwa nthawi ya ku kusala ndi pamene mngelo Gabriele anaonekera kwa Daniele ndipo anamupatsa mauneneri odabwitsa komanso kumvetsetsa zinthu zokhudza Mesiya wolonjzedwayo (v21-23).

Ngakhale kuti kusala sikunalamulidwe kwambiri ndi Mulungu mu Chipangano Chakale, tiona kuti anthu ambiri amene anatumikira Mulungu anali kusala panthawi ya mavuto ndi kusautsika. Iwo anasala kuti machimo ao akhululukidwe, pamene okondeka ao anadwala, komanso kuti apulumutsidwe kwa adani ao. Iwo anasala pamaso pa Mulungu modzichepetsa komanso ndi mtima wosweka pofuna thandizo lake, kukonderedwa kwake ndiponso kulowererapo kwake.

Zitsanzo za Chipangano Chatsopano

Ngakhale kuti Afarisi anasandutsa kusala kukhala ngati goli la kuuzimu, panali ena amene anapitiriza kusala ndi mzimu wofuna kulemekeza Mulungu. Khristu asanayambe utumiki wake, panali Anna, mneneri wamkazi, "amene sankachoka ku Kachisi, wotumikira Mulungu ndi kusala kudya ndi kupemphera usiku ndi usana" (Luka 2:36-37).

Pamene amakonzekera utumiki wake, Yesu "anatengedwa ndi Mzimu kunka kuchipululu kukayesedwa ndi mdierekezi. Ndipo pamene Iye analibe kudya masiku makumi anai usana ndi usiku, pambuyo pake anamva njala." (Mateyu 4:1-3). Nkofunikira kudziwa kuti Mose anasala masiku 40 asanalandire malamulo kuchokera kwa Mulungu. Eliya, amene amaimira aneneri, anasala kwa masiku 40; ndipo tsopano Khristu, nkhoswe ya Chipangano Chatsopano, nayenso anasala kwa masiku 40. Ngakhale ndi malo okhawa pamene akutiiza zakuti Khristu anasala, Yesu anasiyira chitsanzo cha kudzikana chakudya chathupi kuti alandire koposa chakumwa chauzimu cha chikho cha utumiki chimene chinaikidwa patsogolo pake. Khristu analimbikitsidwa ndi kukonzekeretsedwa kumenya nkho, ngakhale panthawi ya mayesero, panthawi yake ya kusala komanso kupemphera kwa Mulungu.

Kunalangizidwa ndi Khristu momveka bwino

Ngakhale kuti sikunalamulidwe mu Chipangano Chatsopano, kunalangizidwa ndi Khristu momveka ndithu ndipo kunatsimikizidwa kudzera mu zochitika za atumwi ndiponso mu mpingo woyamba. Yesu ananena kuti, "pameneponse musala kudya..." (Mateyu 6:16). Yesu sananene kuti, "Ngati musala." Iye amadziwa kuti anthu amene amamumverawo amadziwa za mchitidwe komanso kufunikira kwa kusala. Iwo amamvetsetsa kuti kusala kunali gawo limodzi la moyo wodzikhuthula la mtumiki wa Mulungu.

Ophunzira a Yohane M'batizi anabwera ndi kumufunsa Yesu: "Chifukwa ninji ife ndi Afarisi tisala kudya kawirikawiri, koma ophunzira anu sasala?" (Mateyu 9:14). Yesu anawayankha kuti, "Koma adzafika masiku, pamene mkwati adzachotsedwa kwa iwo, ndipo pomwepo adzasala kudya." (v 15). Ophunzirawo samasala kawirikawiri monga amachitira Ayuda ena ndipo izi zimapangitsa kuti anthuwo adzikhala ndi mafunso. Pali ziphunzitso zimene zabwera kuchokera pa ndimeyi, koma Yesu sanali womangidwa ku lamulo lililonse kapena mchitidwe wokhudza kusala. Nthawi yonse imene Yesu anali ndi ophunzira ake, iwo samafunikira kuti asale, popeza anali pamaso pa mfumu, koma Yesu atabwerera kwa Atate, "ndipo pomwepo adzasala kudya." Yesu atakwera kunka kumwamba, timamva ndithu kuti mpingo unasala ngati gawo limodzi lakudzipereka pofunafuna Mulungu.

Chifukwa cha mphamvu yakumwamba

Pa nthawi ina, ophunzira a Yesu anakanika kutulutsa mzimu woipa mwa mwana wina. Yesu anawalangiza za kufunikira kwa chikhulupiriro ndipo anapitiriza kunena kuti, "Koma mzimu ngati uwu mungautulutsa pokhapokha mutapemphera ndi kusala kudya." (Mateyu 17:14-21, Marko 9:17-29). Kutengera pa malemba amenewa, panthawi imeneyi ophunzira samadziwa machitidwe ake pakusala komabe amatulutsa mizimu yoipa ndi kuchiritsa matenda osiyanasiyana. Yesu amafuna kutsindika kufunikira ndiponso phindu la chikhulupiriro. Iye anayitenga nthawiyi ngati mwai wake wowaphunzitsa ophunzirawo, makamaka pofuna kuwalozera ku nthawi imene iye adzakhale kuti wawachokera, salinso nao limodzi kuthupi. Mlingo wa chikhulupiriro umene unali woyenera kuti munthu akhale ndi mphamvu zoterezi ukhoza kupezeka pamene munthu walumikizana ndi Mulungu mozama mu kusala ndi kupemphera.

Saulo anasala

Yesu atadziulula kwa Saulo pa njira yopita ku Damasiko ndipo Sauloyo ndikutumidwa kuti akalalikire uthenga wabwino kwa anthu amitundu ina, Sauloyo anasala kwa masiku atatu (Ntchito 9:9). Iyino inali nthawi imene amamukonzekeretsa pa utumiki wake ndipo analandira pa moyo wake kudzodza kochokera kwa Mulungu kumwamba. Mtumwi Paulo anadizonetsera yekha ngati mtumiki wa Mulungu posala kwambiri (2 Akorinto 6:4-10). Iye anataya zinthu zosakhalitsa zamoyo uno komanso zathupi pofuna kudzipereka yekha kwathunthu kwa Mulungu nafunafuna mphamvu yake ndi kudzodza kwake.

Mpingo woyamba ufunafuna chitsogozo

Pamene mpingo wa ku Antiokeya unapembedza Ambuye "ndi kusala chakudya, Mzimu Woyera anati, Mundipatulire Ine Barnabasi ndi Saulo ku ntchito imene ndinawaitanirako. Pamene, m'mene adasala chakudya ndi kupemphera



"Yesu anati, 'Ndipo pamene musala ...' Zimadziwikiratu kuti kusala linali gawo limodzi la moyo umene uli wa mtumiki wa Mulungu wodzipereka."

(Yapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)

ndi kuika manja pa iwo, anawatumiza amuke.” (Ntchito 13:2-3). Apa pali chitsanzo cha mpingo woyamba ukusala ndi kupemphera. Inali nthawi imeneyo pamene Mzimu Woyera anawaitanira ku utumiki. Atapitiriza kusala ndi



kupemphera, anaika manja pa anthu awa powaikiza ku ntchito yakumwambayi. Mipingo ya ku Galatiya inapatula akuluumpingo pa kusala ndi kupemphera (Ntchito 14:23). Ha! Ndikadakonda kuti anthu a Mulungu masiku ano naonso atakhala ndi kukhudzika komanso kudzipereka kotereku kokhudzana ndi maitanidwe a Mulungu. Kusala kwao kumaonetsa kuti analidi ofunitsitsa ndi okonzeka kuti Mzimu Woyera awatsogolere pa chilichonse chimene amachita. Ngati mpingo wathu lero ukufuna mphamvu ndi kudzoza ngati kwakaleko, zidzatengera kudzipereka ndi kudzikhuthula pofunafuna Mzimu Woyera.

Kusala Lero

Kusala si chinthu chimene chimangochitika mu Chipangano Chakale chokha basi komanso chimachitika ndi mpingo wa mu Chipangano Chatsopano. Ngakhale kuti sichili chinthu chokhala ngati goli kapena choonetsera uzimu chifukwa ndi chinthu choonetsa kudzikhuthula, kusala ndi gawo limodzi losonyeza moyo wodzipereka. Kusala ndi chisankho

cha munthu ndipo chikuyenera kutsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu pozindikira kuti ifeyo timafunitsitsa kuti Mulungu achitechite ndi miyoyo yathu. Zilipo nthawi zimene tikhoza kusala monga gulu ngati pali chosowa chokhudza tonse potengera zimene ankachita anthu akale. Pamene anthu a Mulungu abwera pamodzi ndi kudzichepetsa mu kupemphera ndi kusala, Satana amanjenjemera. Kusala ndi nthawi yakuti thupi ndi maganizo athu zilozze kwa Mulungu ndipo thupi tilikanize zosangalatsa ndi cholinga chakuti tikhoza kulingalira pa zauzimu.

Kusala si njira yokhotetsera dzanja la Mulungu kapenanso kukhala osadya pofuna kukakamiza Mulungu kuti achite chinachake. Kusala ndi njira yoonetsera kukhumba kwenikweni komanso cholinga. Kukhoza kukhala njira yoonetsera kudzichepetsa komanso nyengo yofunafuna mphamvu ya Mulungu. Ikhoza kukhala nthawi ya kukula kwakukulu mu uzimu ndiponso nthawi yakuti Mzimu wa Mulungu adzionetsere yekha potsogolera ndi kudzoza mosiyana ndi m'mene angachitire m'zinthu zina.

Nkofunika kudziwa choonadi chake cha kusalako

Kusala ndi kopindulitsa ngati kuchitika mwakumvera komanso ndi mtima womasuka ndi woona. Mulungu anawadzudza ana a Israele pa 58:3-6 popeza anasala ndi cholinga cholakwika. Iwo anafunsa kuti “Bwanji ife tasala kudya?” Iwo anasala komabe Mulungu sanawayankhe. Mulungu anawauza kuti iwo anasala “kuti mukangane ndi kutsutsana.” Iwo anali kusala kuthupi ndipo amafunafuna zokhumba ndi zofuna zao. Mulungu sanalandire kusala kwao kumene iwo anachita. Nkofunikira kuti kusala kwathu kusamachitike pofuna kukwaniritsa zofuna thupi lathu kapena zimene timazilakalaka. Kusala kudzikhala nthawi yolingalira ndi yachilungamo. Mulungu sadzalemekeza kusala kongochitika pofuna kukwaniritsa mwambo kapena kongotsatira ndondomeko za anthu. Mulungu anafunsa funso lina pa Zekariya 7:5-7. “Muja mukasala...kodi mukasalira Ine, Inedi?” Anthuwo anali kusala komanso ndi kumakhala m'moyo wosamvera. Kupembedza kwao kunali kwa chiphamaso monga momwe zikuchitikiranso masiku ano pamene anthu akusala koma sakumvera Mulungu mu magawo ena a moyo wao. Kumeneko ndiko kusala kodzilungamitsa kwa Afarisi.

“Ndipo pameneponse musala kudya, musakhale ndi nkhope yachisoni, ngati onyengawo; pakuti aipitsa nkhope zao, kuti aonekere kwa anthu kuti alimkusala kudya. Indetu ndinena kwa inu, Iwo alandiriratu mphotho zao. Koma iwe, posala kudya, dzola mutu wako, ndi kusamba nkhope yako: kuti usaonekere kwa anthu kuti ulikusala kudya, koma kwa Atate wako ali m'tseri: ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe.” (Mateyu 6:16-18).

Ndi chinthu aliyense amachimva mwayekha

Kusala ndi chinthu chimene aliyense amapanga payekha ngakhale kuti kusalako kuli kwa iyeyo ngati munthu kapena kuli kwa gulu. Kumayenera kuchitika ndi maganizo abwino komanso modzigwira polingalira kuti thupi lathu lili kachisi wa Mulungu. Zitsanzo za kusala ndi kupemphera zikupezeka mu Chipangano Chakale ndiponso mu Chipangano Chatsopano. Ngati anthu a Mulungu afunafuna Ambuye ndi mtima wonse komanso mosalekeza pamene akusala ndi kupemphera, kodi ndi zotheka kuti mphamvu ya Mulungu ikhoza kuonekera mwanjira ina yaikulu? Kodi zinthu zimene takhala tikuzilephera tikhoza kuzigonjetsa? Kodi alipo matenda amene akhoza kuchiritsidwa? Nanga alipo mafunso amene akhoza kuyankhidwa? Kodi tikhoza kuona zizindikiro zazikulu komanso kuchuluka kwa chidzalo cha kudzoza kwa Mulungu?

“Koma ngakhale tsopano, ati Yehova, munditembenukire Ine ndi mtima wanu wonse, ndi kusala, ndi kulira, ndi kuchita maliro; ...ndi kutembenukira kwa Yehova Mulungu wanu; pakuti Iye ndiye wachisomo, ndi wodzala chifundo, wosapsa mtima msanga, ndi wochuluka kukoma mtima” (Yoweli 2:12-13).

Mkwati salinso padziko lino lapansi mwathupi, ndipo tsopano ndiyo yakuti ophunzira ake asale! ■



Kodi munthu asale kotalikana motani?

Chipangano Chatsopano sichipereka ndondomeko za kotalikana kwa nyengo imene munthu akhoza kusala. Mfarisi uja pa Luka 18:11-12 amasala kawiri pa sabata. Pa nthawi ya Khristu, Afarisi anali atсандutsa mwambo wosala ngati goli la lamulo. Langizo labwino likupezeka pa Agalatiya 5:18: “Ngati Mzimu akutsogolerani, simuli omvera lamulo.” Tikuyenera kutsogozedwa ndi Mzimu pa kotalikana kwa m'mene ife tingasalire. Pali ngozi yaikulu pamene chinthu chochitika kawirikawiri ku uzimu chisanduka chinthu chongochitika mwa mwambo koma popanda chauzimu chenicheni. Kusala, kaya ndi kochitika pafupipafupi kapena mwapatalipatali, kudzikhala chisankho cha munthu pakati pa iye ndi Mulungu. Kusala kusachitike ngati mwambo wongochitika pa mpingo. Anthu ena thanzi lao lawonongeka chifukwa anasala pafupipafupi kapena kwa nthawi yaitali. Chimenechi si chinthu chabwino ndipo si kusamalira

koyenera kwa thupi lathu monga kachisi wa Mulungu.

Nkofunikira kwambiri kuti tiyesetse kufunafuna Ambuye pa kusala ndipo tisapeputse phindu ndi kufunikira kwake. Yesu ananena kuti ophunzira ake adzayenera kusala, zimene zikutanthauza kuti ife ngati tili ophunzira ake, tikuyenera ndithu kusala. Kusala kwina kudzychitika chifukwa cha chinthu chomwe chachitika panthawiyu. Palinso phindu lalikulu pamene tipatula nthawi pa sabata kapena pamwezi kuti tichite chinthu chauzimu ndi kudzipereka kwa Ambuye mu kusala ndi kupemphera. ■

Kodi ndi mtundu wotani wa kusala umene tikuyenera kutsatira ndipo kwa nthawi yotalika bwanji?

Ichinso ndi chisankho pakati pa munthu ndi Mulungu, popeza kusala ndi mphatso imene munthu amachita mwakufuna kwake. Kaya ndi kusala kwa chakudya, kaya kwa chakudya ndi madzi kapena kwa zakudya zongosankhika, zonsezi zichitike mofulumizidwa ndi Mzimu ndiponso ku ulemmero wa Mulungu. Kotalika kwa kusala kumatengera m'mene Ambuye akukutsogolera. Mose, Eliya ndi Yesu anasala kwa masiku okwana 40, koma izi zinali zoposera pa mphamvu za umunthu ndipo ambiri sangakwanitse kuzichita. Kusala kwa nthawi yotalika kwambiri kuchitike mosamalitsa ndipo munthu aganizire molingana ndi m'mene thupi lake lilili.

Mfumu inasala chifukwa cha Daniele kwa usiku umodzi (Daniele 6:18) popeza imeneyo inali nthawi ya chosowa. Estere anawapempha Ayuda kuti asale kwa masiku atatu

usana ndi usiku. (Estere 4:16). Kusala nthawi zambiri m'malemba kumene kumachitika pakati pa Ayuda kunali kwa tsiku limodzi kuyambira kutuluka kwa dzuwa mpaka kulowa kwa dzuwa. (Oweruza 20:26, 2 Samuele 3:35) ndipo chakudya chimadyedwa madzulo kutada. Kusala kwina kumachitika kuyambira pa kulowa kwa dzuwa lero kufikanso pa kulowanso kwa dzuwa kwa tsiku linalo. Pali nthawi zina pamene munthu akhoza kusala chakudya cha m'mawa, masana kapena madzulo chokha pofuna kuti adzipatulire nthawi yokhala ndi Ambuye.

Kusala kutanthauza kusiya chakudya chathupi pofuna kudya chakudya chauzimu. Pali phindu lochepa pamene tisiya chakudya ndipo kenaka nkudzadya chakudya chochulukirapo panthawi inayo ya chakudya. Chinthu chofunikira kwambiri ndicho chakuti mzimu wathu ulumikizane ndi Ambuye. Kusala kukhale kosankhidwa ndi Mulungu kuti tikweze ndi kumulemekeza Iye pofuna kuti tikwaniritse chifuniro chake champhamvu. ■

Kumasulira Baibulo m'njira ya Interpolation

Mau akuti Interpolation amaimira kuika chinthu cha mtundu wina kapena chosiyana mu chinthu chinzake. Mabaibulo ena amatchula za kusala mu Mateyu 17:21, Marko 9:29, ndi 1 Akorinto 7:5. Komabe, ambiri amakhulupirira kuti ndime zimenezi zokhudza kusala zinachita kuonjezedwa pambuyo, ndipo sizinali gawo limodzi la zolembe za Baibulo zenizeni zoyambirira.

Ndime za pa Mateyu 17:21 ndi Marko 9:29 zikunena za ophunzira kuti sanathe kutulutsa mzimu woipa, ndi Yesu anati, “Koma mzimu ngati uwu mungautulutse pokhapokha mutapemphera ndi kusala kudya.” Malingana buku lolongosolera la Adam Clarke Commentary komanso akatswiri ena a Baibulo, ndime ya Mateyu 17:21 siili mu gulu la mabuku akale otchedwa Vatican MS, amene ndiye akale kwambiri komanso ndiye odalirika kwambiri mwa mabuku ena onse akale. Ndimeyi siipezeka mu mabuku ambiri akale amene ali odalirika. Ngakhale kuti mabuku ena akale ali ndi mau akuti “Kusala” makamaka mu buku la Marko, gulu la mabuku akale la Vatican Manuscript limasiya mau akuti “Kusala”, ndipo Amplified Bible limaika mauwa akuti “ndi kusala

chakudya,” mopenekera komanso mamasulidwe ena a Baibulo samavomereza choonadi chake. Tchutchutchu wake wa mtsutso wokhudzana ndi ndimeyi sutherapo. Chosangalatsa nchakuti mabaibulo onse amene ali mu zinenero zimene Kalata ya Uthenga Wabwino imasindikizidwa, amagwiritsa ntchito mau a kusala ku uthenga wa Mateyu. Chinenero cha chi Swahili sichimagwiritsa mau akuti kusala mu uthenga wa Marko.

Pa 1 Akorinto 7:5 akukakamba za abambo ndi amai osakhilira malo amodzi kwa kanthawi chifukwa ndicholinga chakuti apemphere ndi kusala. Mau akuti kusala sanaikidwe mu mabuku akale ndipo otanthauzira ambiri saikamo ndime imeneyi. Buku lolongosolera la Jamieson, Fausset, ndi Brown Bible Commentary likunena kuti mau akuti “Kusala” anali ongosomekerapo, makamaka ndi iwo okonda kukhala m'moyo wodzipatula pochita zauzimu. Mabaibulo a chinenero cha chi Spanish ndi chi Swahili samaika mauwa akuti “Kusala” ndipo akupezeka mu mabaibulo a zinenero za chingerezi ndi chi German.



KODI MUKUDZIWA?

Nyengo ya Lenti pakati pa akhristu ndiyo nthawi yapadera yopemphera, kusala, kulapa, kupereka nsembe, ndiponso kuchita ntchito zabwino pokonzekera chikondwerero cha kuukitsidwa m'manda kwa Ambuye Yesu. Lenti ndi nyengo imene imakumbukiridwa kwa masiku 40, koma si chiphunzitso cha Baibulo. Ena amalimbikitsa kusala kwa pa nyengo ya Lenti pokumbukira kusala kwa Khristu m'chipululu muja, komabe izi sizigwirizana ndi chikhalidwe cha mpingo wa nthawi yakale. Pali umboni wambiri wakuti anthu mu mpingo

woyamba anasala pafupifupi maora 40 amene Yesu anakhala ali m'manda - komabe m'zina zolembe za mpingo oyamba, zimenezi sizipezeka. Ena amaphunzitsa kuti kusala kudzikhala kwa tsiku limodzi, ena masiku awiri ndipo ena amati oposerapo. Sitidziwa kuti zinakhala bwanji kuti mpakana anthu adzikumbukira nyengo ya Lenti, ngakhale kuti machitidwewa anakhazikika utachitika msonkhano waukulu wa ku Nicaea m'chaka cha 325 AD. Maora 40 aja kenaka anakhala masiku 40 a kusala, ndipo ngakhale zinali choncho, tanthauzo la kusala linasulutsidwa ndipo linaphatikizanso kusiya zinthu zina osati chakudya chokha.

Anthu a Mulungu sali womangika ku chopusa kapena ukapolo wa chipembedzo chamunthu, koma pokhala oyera mtima a Mulungu, iwo akuyenera kukhala m'moyo wopitirira kudzipereka kwa Mulungu. ■



**Mau a
Nyengo
Yake**

KUPEMBA MULUNGU

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

Ndipo Mose anapemba kwa Yehova Mulungu wake —Eksodo 32:11

Pamene Mose analandira malamaulo kuchokera kwa Mulungu pa phiri la Sinai ndipo anatsika paphiri paja, iye anazindikira kuti anthu anasiya Mulungu ndipo tsopano amapembedza mwanawang'ombe wosema. Mkwiyu wa Mulungu unalilima, ndipo Iye anauza Mose kuti adzawaononga anthuwo. Mose anapemba Ambuye ndipo anawapembedzera anthuwo kuti Mulungu awachitire chifundo komanso kubweza mkwiyo wake.

Chifukwa chakuti Mose anadzichepetsa pamaso pa Ambuye ndipo anapempha chifundo ndi kukoma mtima kwake, Mulungu anasintha maganizo ake nawasiya Aisraele osawaononga. Mose akanakhala kuti sanapemphe moona mtima kwa Mulungu kuti achepetseko chiweruzo chake, ana onse a Israele akanaanongeka ndipo Mulungu akanadzuka mtundu wina kuchokera mu mbeu ya Mose.



Njira za Mulungu ndi zangwiro ndi zolungama, komabe Iye ndi Mulungu ndipo amagwidwa ndi chifundo pamene olungama anthu oyera mtima ayitanira pa dzina lake. Mulungu anasintha maganizo ake ndipo kangapo konse anabweza zimene anafuna kuchita chifukwa chakuti wina wake anapemba Mulungu.

Mulungu amalemekeza mapemphero ndi kusala kwa anthu ake ndiponso amakhudzidwa pa mpando wake wachifumu pamene oyera mtima afuulira kwa Iye kuti athandize ndi kulowererapo. Ngakhale pamene aweruza anthu osalungama, nthawi zambiri Mulungu amawachitira chifundo ndipo amachedwetsa chiweruzo chake pamene wina wokhala ngati Mose amupemba Iye. Limeneli ndiye phindu la pemphero lopembedzera. Mdaniyo amafuna kutipangitsa kuti tidziganiza zakuti chochitikacho chikhoza kuchitika ngakhale titati tisapemphere. Zinthu zimene zinachitika kale ngakhale zochitika pano zimatsimikiza ndithu kuti Mulungu kumwambako akumvetserabe ku mapemphero a anthu ake. Chifukwa cha ichi, tiyeni tipemphere ndipo tisafooke. Tiyeni tilemekeze ndi kupindula ndi mwai umene timakhala nawo pa pemphero makamaka pozindikira kuti ilo limatisendezera ife kwa Mulungu, komanso kutithandiza kuti tisinthe moyo wina umene uli wotaika pamene Mulungu wachedwetsa chiweruzo chake chifukwa cha mapemphero a mmodzi mwa ana ake okhulupirika. ■

CHIYERO CHA KWA AMBUYE